PHUNZIRO LA 53

1.Kodi chifukwa chiyani Yesu anali ndi udindo wokhuluruka tchimo?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.

2. Kodi chifukwa chiyani Yesu ankatha kuŵachiza anthu odwala?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.

3. Kodi dzina lachiŵiri la Levi linali ndani?
-Mateyu.

4. Kodi tchito ya Mateyu inali yotani pamene Yesu anamuyitana kuti amutsate iye?
-Mateyu anali okhometsa msonkho.
-Mateyu ankaŵakhometsa msonkho anthu ache a Chiyuda ndikumaŵapatsa Aloma.

5. Kodi Yesu anabwera kudzapulumutsa ndani?
-Yesu anabwera kudzapulumutsa anthu okhawo amene akudziŵa kuti aŵachimwira Ambuye, ndipo Mulungu yekha ndi amane angathe kuŵapulumutsa iwo.

-Tsiku lina Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo anamufunsa Yesu kuti aŵawonetse chizindikiro chozizwitsa.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 12:38

38-Kenako Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo anati [kwa Yesu], “Mphunzitsi, tikufuna kuti tiwone chizindikiro chozizwitsa kwa Inu.

-Kodi Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo ankafuna kuwona chiyani m'malo moŵakhulupilira Mawu a Mulungu?
-Ankafuna kuwona chizindikiro chozizwitsa.

-Kodi chifukwa chiyani Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo anapenpha kuti aŵawonetse chizindikiro chozizwitsa?
-Kodi iwowo sankamva kapena kuwona kuti Yesu anatulutsa ziŵanda mwa anthu?
-Ankamva ndiponso kuwona.

-Kodi iwowo sankamva kapena kuwona kuti Yesu anamuchiza munthu wa khate?
-Anamva ndiponso kuwona.

-Kodi iwowo sankamva kapena kuwona kuti Yesu anamuchiza munthu wa manjenje?
-Anamva ndiponso kuwona.

-Kodi iwowo sankamva kapena kuwona kuti Yesu anaŵachiza anthu onse amene ankabwera kwa Iye?
-Anamva ndiponso kuwona.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo ankafuna kuti adziwonetsedwabe zizindikiro zozizwitsa zambiri?
-Chifukwa chakuti sankakhulupilira kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi.

-Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo ankangofuna kuti adziwona zizindikiro zozizwitsa zokhazokha m'malo mokhulupilira mwa Yesu.



-Ngakhale kuti chiphunzitso cha Yesu chinali choposa cha Yona, Ayuda anakanabe kukhulupilira.

-Ngakhale kuti Yesu anapanga zizindikiro zozizwitsa zambiri zimene Yona sanathe kuchipanga, Ayuda anakanabe kukhulupilira.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu ananena kuti Ayuda ndi oyipa kwambiri kuposa anthu a ku Nineva?

-Chifukwa chakuti anthu a ku Nineva anatembenuka mitima yawo chifukwa cha chiphunzitso cha Yona koma Ayuda sanatembenuke mitima yawo ndi chiphunzitso cha Yesu, Mulungu Mpulumutsi.

-Ngakhale kuti Yesu anaŵaphunzitsa Ayuda kuti atembenuke mitima yawo ndipo anachita zizindikiro zozizwitsa zambiri, Ayuda anakanabe zakuti Yesu ndi Mulungu Mpulumutsi.

ndipo anatembenuka mitima yawo.

-Kodi anthu a ku Nineva ankaŵadziŵa malonjezo a Mulungu amene anaŵapereka kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo?
-Iyayi.

-Kodi anthu a ku Nineva ankaŵadziŵa malamulo onse amene Mulungu anaŵapereka kwa Mose?
-Iyayi.

-Kodi anthu a ku Nineva ankazidziŵa zizindikiro zozizwitsa zonse zimene Mulungu anachita kwa a Isirayeli?
-Iyayi.

-Ngakhale kuti anthu a ku Nineva sankadziŵa china chilichonse pa zimenezi, iwo anatembenuka mitima yawo Yona atafika kwa iwo.

-Tsopano wina opambana Yona ankaŵawuza anthu kuti atembenuke mitima yawo.

-Kodi opambana kuposa Yona ndi ndani?
-Yesu, Mulungu Mpulumutsi.

-Kodi Yesu anali opambana bwanji kuposa Yona?

-Yona anali munthu koma Yesu anali munthu komanso Mulungu weniweni.

-Ngakhale kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi ndipo Yona anali munthu, Ayuda anakanabe kukhulupilira.



-Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo ankangofuna kuti adziwona zizindikiro zozizwitsa zokhazokha m'malo mokhulupilira M'mawu a Mulungu.

-Kodi mukuzikumbukira zozizwitsa zambiri zimene Mulungu anaŵawonetsa a Isirayeli koma sana-khulupilirebe?

-Mulungu anatumiza milili khumi kwa Farawo ndi a Iguputo, koma a Isirayeli sanakhulupilirebe.

-Mulungu anamumiza Farawo pamodzi ndi asilikali ache M'nyanja Yofiira, koma a Isirayeli sanakhulupili-rebe.

-Mulungu anatumiza zimziri ndi mana kwa a Isirayeli m'chipululu muja, koma a Isirayeli sanakhulupilirebe.

-Anthu ambiri amafuna kuti adziwona zizindikiro zozizwitsa m'malo mokhulupilira mwa Yesu.

-Koma kuwona zizindikiro zozizwitsa sikungatipu-lumutse ife.

-Kukhulupilira mwa Yesu Mpulumutsi kokha ndi ku-mene kungatipulumutse ife.

-Ngati tikuganiza kuti tikhoza kukhulupilira mwa Yesu tikawona chizindikiro chizizwitsa, ndiye kuti tikumutcha Mulungu kuti ndi wabodza.

-Ngati tikuganiza kuti tikhoza kukhulupilira M'mawu a

Mulungu tikawona chizindikiro chizizwitsa, ndiye kuti tikuŵatcha Mawu a Mulungu kuti ndi abodza.

-Kodi Yesu anaŵayankha chiyani Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo aja?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 12:39

39-Koma Iye anaŵayankha kuti, "Obadwa ali oyipa ndi achigololo afunafuna chizindikiro chozizwitsa! Ndipo palibe chizindikiro chimene chidzapatsidwe kwa iwo, koma chizindikiro cha Yona Mneneri chokha."

-Kodi Yesu anayankha kuti chiyani?
-Yesu anayankha kuti anthu oyipa ndi achigololo okha ndi amene amapempha kuwonetsedwa chizindikiro chozizwitsa.

-Kodi chizindikiro chozizwitsa chimene Yesu anapereka kwa anthu chinali chotani?
-Chizindikiro chozizwitsa cha Yona.

-Kodi chizindikiro chozizwitsa cha Yona chinali chotani?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 12:40

40-[Yesu anati] "Pakuti Yona anali m'mimba mwa chimsomba masiku atatu ndi usiku wache, chomwechonso Mwana wa munthu adzakhala mu mtima mwa dziko la pansi masiku atatu ndi usiku wache.



-Kodi chizindikiro cha Yona chinali chotani?
-Ngati m'mene Yona anakhalira m'mimba mwa chimsomba masiku atatu ndi usiku wache, chomwechonso Yesu adzakhala m'mimba mwa dziko la pansi masiku atatu ndi usiku wache.

-Ngati m'mene Mulungu anamutulutsira Yona m'mimba mwa chimsomba patatha masiku atatu ndi usiku wache, chomwechonso Mulungu adzamuturutsa Yesu m'mimba mwa dziko la pansi patatha masiku atatu ndi usiku wache.

-Yesu ankaŵawuza Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo kuti chizindikiro cha Yona chinali chizindikiro chakuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani kwa Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 12:41

41-[Yesu anati] "Pa tsiku lolamulidwa anthu a ku Nineve adzayima pamodzi ndi anthu a m'bado uno, ndipo adzidzaŵayimba milandu; chifukwa chakuti iwo anatembenuka mtima ndi kulalikira kwa Yona, ndipo tsopano oposa Yona ali pano."

-Yona anapita ku Nineva kwa anthu oyipa ndikukaŵawuza kuti atembenuke mitima yawo ndipo ngati sakutelo, Mulungu adzaŵalanga.

-Kodi anthu a ku Nineva anachita chiyani?
-Anamvera Mawu a Mulungu kudzera mwa Yona